


**NKHANI YABWINO KWA OSAUKA**



**YESU, NDINE WOPANDA CHIYEMBEKEZO.**

**CHONDE THANDIZENI**

Ndine wosauka.Banja langa ndilosauka.Sindingathe kubweza ngongole zathu.Ana anga sakupitanso ku sukulu chifukwa ndilibe ndalama zokwanira zolipilira sukulu.

Tikadwala sitikwanitsa kukaonana ndi dotolo .Nthawi zambiri timadya kamodzi patsiku.

Ndalama yolipilira nyumba yakhalitsa tisanapeleke.Ndikukanika kubweza ngongole yomwe ndinabwereka.

Palibe yemwe akufuna kundithandiza .Ndine wopanda chiyembekezo.Nanga ndingatani ?

- \*kupempha ndalama kumseu?
- \*Ndikatchove juga?
- \*Ndikachite zosayenera kuti ndipeze ndalama?
- \*Ndikajowine athu azisokonezo?
- \*Ndikalowe mdziko lina mwachinyengo kuti ndikapeze ntchito ndi ndalama?

Nkovuta kuti ndithandizike .  
Kodi chilipo China chomwe ndingachite?

Kodi **Gandhi** adachita Chiyani?

Pamene Gandhi adakomana ndi zovuta,pamene sadakatha kusintha za kunja kwa moyo wake,sadaganize zochita chisokonezo kapena mchitidwe waumbanda.

Koma adayang'ana mkati mwa moyo wake ndi kusintha za mkati mwamoyo wake.

Adafufuza moyo wake,nasintha pokhala munthu wabwino:

Pokhala okoma mtima ,okhulupilika,othandiza ena,kuchepetsa kudzikaikira,nkhanza,kuganiza zoyipa ndi kuyesera kutsuka mtima wake.

Ndipo chidachitika ndi chiyani?pamene adasintha moyo wake ,zitseko zidayamba kutsekuka .Zakunja kwa moyo wake zidayamba kusinthanso.Gandhi adapeza kuti kusinthika kwa moyo wake mkati ndi njira yamphamvu yosinthira zochitika za kunja kwa moyo wake.



Kodi **Mandela** adachita Chiyanti?

Mandela adakhala mu ndende zaka 27 mumazunzo. Nthawi zina samalandira ngakhale kalata kwa miyezi isanu ndi umodzi .Kamodzi adayikidwapo m'manda ndipo alonda adamukodzera. Adakhala mumoyo woyipa komanso wankhanza zedi.

Koma adakhalabe olimbika mtima. Adapitilira kukonza moyo wake ndi kudzisintha poyesera kuwerenga mabuku ndi kukhululukira amene adamulakwira.

Mtima wake udayamba kukhala wabwino ndi opambana.

Atamasulidwa kundende ndi kuzipyinjo adafika pa chiyindeyinde cha ubwino nakonza ndi kuyanjanitsa dziko lake.

Kodi **Yesu** adaphunzitsa Chiyani?

Kuyankhula kwa anthu osauka kwambiri, amene adali ovutika ngakhale kuti apeze chakudya cha tsiku kunali kovuta. Anthu amene amakhala mu ulamuliro wa nkhanza wa chi Roma, Yesu sadawauze kuti :

- "Chitani nkhondo ndi Aroma".
- sadati "chitani chisokonezo kuti mupeze chulungamo Chanu".
- sadati "patani ndalama kunyumba ya juga"
- sadati "abeleni olemera".

Sadawauze kuti achite ntchito zathupi.

Koma adawauza osauka kuti:

- \_ apewe umbombo ndi kukhudzidwa ndi ena.
- \_ apewe kusilira ndi kuonetsa chifundo.
- \_ apewe mtopola ndi kukhala okhululuka.

Yesu adawauza osauka kuti akhazikike pa zosoweka za moyo ndi kuganizira moyo wawo poyamba ndi kusintha moyo wawo ngati njira yopangitsa moyo wawo kukhala wabwino ndi dziko lawo.

Yesu kamodzi adanenapo chopambana ichi;kwa osauka ndi osowa.

"Siyani kudandaula kwambiri za chakudya ndi zovala.Ganizilani za Mulungu poyamba ndipo chakudya ndi zovala sizidzakhala vuto".

Uku ndi kuyankhula kosintha zinthu.

-----

Anthu ena atha kunena kuti "mayiko olemera ayenera kuthandiza mochuluka mayiko osauka".Inde ayenera .Komanso ngakhale anthu olemera m'mayiko osauka ayeneranso kuthandiza mzika zinzawo kwambiri.

Koma nzovetsa chisoni dziko lathu lovuta ili likuvutika pa chimene Pope Francis akuchitchula kuti "kusayanjanitsika kwa dziko lapansi". Ambuye lolani kuti Kusayanjanitsika kwa dziko lonse lapansi ndi umbombo zichoke ndipo pakhale kuyendelera kwa Mzimu wa chifundo ndi kusamalirana.



Mwakumvetsa kwawo anthu osauka atha kunena kuti "Maganizo amenewa mnzongokamba, sizigwira ntchito, Maganizo amenewa angandithandize ine bwanji kuti ndikhale ndi chakudya pagome langa kapena kundithandiza kupereka malipiro a sukulu kapena sukulu fizi. Banja langa silingadye Maganizo ndipo maganizo sangapereke sukulu fizi.

Chabwino, mvetserani nkhanu ya **Samu** iyi; Samu adakulira mu umphawi mdera lina lalikulu.. Ngakhale amagwira ntchito molimbika maola ambiri, iye ndi mkazi wake samatha kupereka zofunika kwa ana awo anayi. Opanda ndalama zokwanira za chakudya, sukulu fizi kapena ndalama zolipilira kuchipatala.

Samu ndi mkazi wake adamva za ganizo losintha moyo wawo ngati njira yosinthira moyo wathupi. Samu adasiya kusuta (adali osuta Zedi). Adasiya kumwa kachaso. Adasiya njuga. Adayamba kukhala panso ndi banja lake. Mkazi wake adasiya miseche yapaabale awo ndi azinzawo. Adayamba kuthandiza mzimayi wokalamba amene amakhala naye ndipo adalibe banja. Usiku uliwonse banja lonse limapemphelera pamodzi ndi kukhala ndi chidaliro chatsopano mwa Mulungu.

Mwadzidzidzi zinthu zidayamba kuchitika;matenda adachepea m'banja la Samu.Samu mwini adakhala wathanzi ndipo adapeza ntchito yomwe amalandira malipiro abwino.Chisamaliro chomwe mkazi wake amapereka kwa mzimayi wamasiye chinakopa chidwi cha mzimayi woyandikana naye yemwe adali wochita bwino amene adamupatsa ntchito yapadera yokonza chakudya mu resitanti yake.

Ndi ndalama zimene adazipeza pa ntchito yatsopano Samu ndi mkazi wake sadali chabe kungotha kupereka chakudya chokwanira kwa ana awo.Adakwanitsanso kupereka fizi ya sukulu kwa mwana wawo woyamba. Mwana oyamba uyu adalandiranso ulemu wapadera kuchokera kwa mphunzitsi pasukulu amene payekha adalipiranso Sukulu fizi ya mwana wachiwiri.

Pamene wachibale wa mkazi wa Samu adakawachezera kuchokera gawo lina la dzikolo,adasangalatsidwa ndi kusintha komwe adakupeza pabanjapo.Kotero adatenga udindo wolipirila ana awiri otsalawo.

Samu ndi banja lake adazindikira kuti ubwino umabweretsa zabwino ndi kusintha kwakukulu pa moyo wa munthu.



**Chenjezo:**

Samalani ndi zotchedwa "Uthenga wotchukitsa" .....umene umati "Khulupilirani Mulungu ndipo mulemera".

Anthu okhawo amene amadzilemeretsa ndi chiphunzitso chabodza ichi ndi Abusa abodza amene amagwiritsa ntchito zithandizo zochokera kwa osonkhana awo kapena mamembala kuti agule magalimoto odula, manyumba odula ndi ndege. Monga T.B Joshua "Mbusa wa chisanu ndi chimodzi kulemera ku Nigeria".

Yesu sadanene kuti ophunzira ake adzakhala olemera ndi zinthu pa dziko lapansi. Adanena kuti adzakhala olemera kumwamba. Adati adzapatsidwa zosowekera za moyo wawo ndi kudziwa mtendere m'moyo uno ngakhale kunzunzidwa.

-----

Kwa amundende ,ovutika kundende ya colombia .Pope Francis adati ngakhale ali moteremu iwo ali ndi kuthekera kosintha zinthu\_Mariya amene adasintha moyo omvetsa chisoni kukakhala nyumba ya Yesu.

Samu ndi mkazi wake adazindikiranso kuti pokhazikika pa zinthu zamuyaya ,kutanthauza kuti Kusiya zakale zomwe amakhala ndi kuchitapo kanthu.Sizitanthauza kungokhala chete ndi kumalota ndikufuna kuti zinthu kapena mavuto angotha okha mwamatsenga.

Uku sikunena kuti anthu onse osauka ndi aulesi,ongogona.koma ena chabe.Ena amayembekezera ndalama kuti zingogwa kuchokera kumwamba kopanda kugwirira ntchito.

Baibulo likufotokoza malo ambiri za ulesi kwenikweni polumikiza ulesi ndi umphawi.

Izi zitha kumveka mwankhanza kwa anthu ambiri amene abadwira mu umphawi,nthawi zina umphawi umachitika Chifukwa cha mfundo zankhanza za dziko ndi Mayiko pankhani za malonda.

Koma njira yosinthira sikungokhala pansi namanena kuti ndine watsoka .Koma tiyenera kuchoka ku zomwe tidagwira zolakwika ndi kusintha zikhalidwe zathu zoipa.

c.f. "Mulungu kuyitana," October 25:

Njira yogonjetsera  
zinthu izi zosakhazikika ndi kuphunzira  
kugonjetsa moyo wathu omwe, aliyense wa ife.

Funani tsiku ndi tsiku ndi mochuluka kuti  
mugonjetse inu eni ndipo mupambana ndithu  
ngakhale simungathe kuona izo, kugonjetsa  
mphamvu zosakhazikika.

Kusowa kwa ntchito kutha kutha ngati munthu  
azindikira izi;

Ngati sadagwire ntchito adzipange yekha  
kukhala mphamvu yogonjetsa .Poyamba  
kugonjetsa zinthu zonse zoyipa pa iye mwini  
kenako panyumba pake ndi zonse  
zomuzungulira.

Adzakhala mphamvu yomwe idzafunike ndipo  
adzayenera kulembedwa ntchito.



Zaka 100 zapitazo akatswiri a sayansi adayamba kuyankhula za kethekera kwa mphamvu ya atomiki.

Yesu pophunzitsa za kudzigonjetsa akufanizira ndi mphamvu ya atomiki ya uzimu. Itha kubweretsa mphamvu yayikulu mu miyoyo yathu imene sitimayiyembekezera kuti ndikuchitika.

Monga Gandhi ndi Mandela, titha kuzindikira ndi kupita patsogolo ndi mphamvu yositha ya uzimu.

Njira imodzi yokhazikitsira mphamvu imeneyi ndi kupangitsa malingaliro ndi mitima yathu kupewa maganizidwe oyipa, kupangitsa lilime lathu kupewa zoyankhula zoyipa.

Kungokhala tsiku lonse kumadandaula za m'mene zinthu ziliri ndi zopangitsa kuti tisafikire zimene tikufuna; zimangopangitsa kuti zinthu ziyipireyipire.

Kuyesera kukhala osakayika m'maganizo ndi nzoyankhula ndi mphamvu yopangitsa kuti tichite bwino.

Olemba ambiriaza uzimu amafotokoza kuti machitidwe apamwamba a "kuganiza kwaphindu" ndi kutamanda Mulungu. Kutamanda mulungu kumabweretsa kusinthika kwakukulu pa munthu.

c.f. "**Mulungu kuitana**", October 16

Inde! kutamanda. Nthawi imeneyo, pa malo ovuta kwambiri, moyo wanu umasintha kukhala wachimwemwe. Kudandaula kwako kukakhala kutamanda zochitika zako zimasintha kuchokera ku zopanda pake kukhala olongosoka, kuchoka ku chisokonezo kukhala mtendere.

Chiyambi cha kusinthika ndi iwe mwini, komabe uyenera kuonetsetsa zochitika Zako, komabe mochepa utha kupeza mayankho a nkhani zachuma, nthawi zonse utha kutembenukira kwa iwe mwini ndikuona ngati chinachake chasokonekera, kenako ndikukonza chimenecho.

Monga momwe nzofunika kusintha zonse za paiwe, nthawi zonse udzapeza kuti moyo wako wasintha Pochita izi udzamasula mulungu womangidwa. Mphamvu ya mwaiwe. Mphamvu imeneyo ikangoyamba kugwira ntchito, mofulumira imachita zodabwitsa. Kenako zoonadi kulira kwako kudzakhala chimwemwe.

"Chifukwa chiyani Boma silifuna kundithandiza ine,m'mene zimakhalira m'mayiko ena.Chifukwa chiyani Boma langa ndiladziphuphu kwambiri ndi losasamala".

Njira imodzi yosinthira Boma ndi kusintha kwa zochitika za mzika zake.Ngati ndingakhale munthu wabwino ,ndiye kuti zitha kukhala ndi phindu lochuluka ndi kuthandiza dziko langa kukhala malo abwino ngakhale kuti sindingathe kuona kusinthika mofulumira.

Ngati anthu wamba ochuluka angadzisinthe okha ,dera lonse ndiye pang'onopang'ono likhala labwino ndi losinthika.

Chimodzi chomwe ndingathe kuchita ndikupezeka munthawi yake yoyenera!.M'malo ambiri,anthu sasamala zofika mu nthawi yake yomwe apangana;(....."nthawi ya chifrica".....)

Kodi nanga geni,kapena dziko lingapite bwanji patsogolo ngati munthu aliyense sasamala za nthawi?Kupezeka pamalo munthawi yake ndi njira imodzi imene munthu atha kudzisinthira ndi kukwaniritsa kapena kufikira zolinga zake.




Osanena kuti "kundende,nena kuti malo a maphunziro apamwamba"(university).

Atatha kukhala kutali ndi dziko lakwawo kwa Zaka zisanu ndi ziwiriw(7),Simoni adafunsidwa ndi anzake "kodi udachitako chiyani ku Hong Kong".Adayankha."Ndidali ku sukulu yapamwamba(university).Kwa Zaka ziwiri zoyamba ndidasintha chingelezi changa powerenga kwambiri,nthawi zonse kugwiritsa ntchito buku la matanthauzo a mawu (dictionary).Kenaka Zaka zisanu zotsatira ndidatenga maphunziro awiri a ku university.Limodzi la chingelezi ,phunziro lina la m'mene ndingayendetsere geni .Tsopano ndili okonzeka kuyambanso moyo wina ndi nzeru ndi maluso omwe ndidaphunzira".

Monga Mandela, moyo wa Simoni wa matsoka ndi zipsinjo idakhala nthawi ya dalitso.Monga kuyankhula kwachi-China "kulephera ndi chiyambi chochita bwino".

Pa website yanga [www.v2 catholic.com](http://www.v2catholic.com),pali failo ya "**Nkhani yabwino kwa osauka**"ndi nkhani yonse ya bukuli.Ngati mukufuna kupereka ndemanga kapena maganizo anu pa buku limeneli mutha kutumiza email yanu kwa ine pa [jdwoni@gmail.com](mailto:jdwoni@gmail.com).



Khalani osinthika m'mene mufunira kuti dziko  
liwonekere-Gandhi

Alivense atha kufikira pamene akufuna ndati adzipereka  
ndi kukhala ndi kukhumba kotero-Mandela

Mkwabwino kufuna kukhala ndi zokwanira koma  
sikwabwino kufuna kulemera. Anthu amene amalakalaka  
kulemera amakodwa mu msampha wa machitidwe wopusa  
ndi oopsa amene amawononga miyoyo yawo.

ISBN 978-988-12396-3-1

First printing, December 2015

Printed in Hong Kong by Print Shop [www.printshop.hk](http://www.printshop.hk)

For private distribution only. Not for sale

Publisher: Fr John Wotherspoon O.M.I. 胡頌恆神父

Email : [jdwomi@gmail.com](mailto:jdwomi@gmail.com) Tel : +852 67095674

Also in this series : *The Simple Bible* & *Doctor Jesus*

Full texts [www.simplebible.info](http://www.simplebible.info) & [www.doctorjesus.org](http://www.doctorjesus.org)

God bless the kind friends who produced this book